FROM SLAVERY TO NATIONHOOD (Chinyanja)
PUBLISHED BY THE BAPTIST PUBLISHING HOUSE
P. O. BOX 31995, LUSAKA, ZAMBIA

2106

# Kucoka Muukapolo kukhala Pfuko la Anthu




wa Israyeli. Tiyenera kufuna cithandizo ca Mulungu posankhula mtsogoleri.

2. Aisrayeli anafuna mfumu monga mitundu ina. Zomwe anthu ena akucita sizabwino nthawi zonse.



2106



# Kucoka Muukapolo kukhala Pfuko la Anthu

FROM SLAVERY TO NATIONHOOOD
(Chinyanja)

FIRST PUBLISHED
1 January, 1983

BY THE
Baptist Publishing House
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia

PRINTED BY
Baptist Printing Ministry
P.O. Box 31995
Lusaka, Zambia

OLEMBA NDI: Mrs. Carroll Brown

"Aliyense ali kucita zimenezi" ndikhalidwe limene timalipeza kulikonse masiku ano, pakati pa ana acinyamata ndi akuru. Kungoti cifukwa aliyense alikucita kanthu kena sicipanga kuti cinthuco ndi cabwino. Israyeli anafuna mfumu cifukwa mitundu ina inali ndi mafumu. Nthawi zambiri kutsatira gulu ndi cinthu colakwa. Nthawi zina ndi cinthu cabwino. Cikwati cokhala anthu asanakwatilane ndi kulakwa. Cifukwa cakuti ena amacita zimenezo sicipanga kukhala colondola. Anthu ambiri amamwa zoledzeletsa, koma kuteroku sikupanga kuti ndizabwino. Mkristu ayenera kumvera Mulungu. Ngati gulu likutsatira Mulungu, ndikumvera Mulungu, ndikwabwino kulitsata.

Monga taphunzira nthano ya mtundu wa Ahebri taphunzira za malonjezo ophwanyika. Taphunzira kucokera ku maudindo amene tiri nao monga anthu a Mulungu. Tiyenera kufuna funa atsogoleri a Cikristu, amene amamvera Kristu, kutumikira monga atsogoleri aboma. Tiyenera kupempherera atsogoleri aboma lathu, cifukwa taphunzira kuti atsogoleri osadziwa amaononga mtundu. Tiyeni tikhale omvera kwa Mulungu. Tiyeni tipempherere atsogoleri athu kuti adzazidwe ndi nzeru ndi cidziwitso ca Mulungu.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Mulungu afuna kulamula ndi kutsogolera mbali ili yonse ya moyo wanu. Iye amapereka mwai wosankha zomwe mungacite. Kristu ndi mfumu ya Mkristu, komabe ndi bwenzi lace.

ZOMWE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Mulungu anaitana Samueli monga mtsogoleri

Mulungu alankhula kwa Samueli (1 Samueli 8:7-8). Iye anauza Samueli kuti anthu sanamukane. Iwo anakana Mulungu. Iwo anafuna kukhala monga mitundu ina.

Mulungu anauza Samueli kulora kuti Israyeli akhale ndi mfumu. Samueli anacenjeza anthu kuti mfumu idzafuna kuti iwo acite ciani. Iwo adzakhala akutumikira mfumu. Ana ao adzakhala asilikali ace. Iwo adzakhala akupereka ndalama zao ku boma.

SAULI ASANKHIDWA MONGA MFUMU

Mulungu anatsogolera Samueli kusankha Sauli monga mfumu. (1 Samueli 9) Mulungu anabweretsa Sauli ndi Samueli pamodzi.

Sauli adzozedwa monga mfumu (1 Samueli 10:1). "Kudzoza" kumatanthauza kuti anaikidwa pambali pa malo autumiki cifukwa ca nchito. Mulungu anadalitsa Sauli. Samueli anauza Sauli kuti ayenera kucita cifuniro ca Mulungu.

Poyamba, Sauli anakhoza kuteteza adani a Aisrayeli (1 Samueli 13-14). Koma posacedwa Sauli anaiwala kufunika kwa Mulungu.

PHUNZIRO LAMIYOYO YATHU

Mulungu sakakamiza aliyense kuti amumvere iye. Tiri ndi ufulu kusankha kucita zomwe tifuna ndi miyoyo yathu. Ngati ife sitimvera Mulungu, tidzabvutika. Aisrayeli nthawi zonse anabvutika pamene sanali kumvera Mulungu. Ufulu weni weni umakhala ndi amene atumikira Mulungu.



2106

FROM SLAVERY TO NATIONHOOD
(Chinyanja)

PHUNZIRO TSAMBA

1. ANTHU A UKAPOLO....................3
2. MTSOGOLERI AITANIDWA................8
3. LOLANI ANTHU ANGA APITE............13
4. MADYERERO AUFULU...................17
5. MULUNGU AMAPANGA ANTHU APANGANO.....21
6. ANTHU OPEMBEDZA....................25
7. KUSAKHULUPIRIRA KUMACEDWETSA KUKWANIRITSA KWA PANGANO..................31
8. KUKWERA DZIKO LA MALONJEZANO........36
9. MABVUTO POSUNGA PANGANO............40
10. KUKONZANSO PANGANO.................44
11. GIDEONI: MUNTHU WA MULUNGU WOLIMBA MTIMA...............................48
12. KULIMBANA NDI OTSUTSANA............52
13. TIPATSENI MFUMU....................57

ayenera kukhala okhulupirika kwa iye.

Samueli anatsogolera Israyeli kwa zaka zambiri. Ndipo anakalamba. Mtsogoleri anayenera kusankhidwa kuti atenge malo ace.

(Werengani 1 Samueli 8:1-9; 10:10)

SAMUELI ASANKHA ANA ACE

Ndime 1 ikunena kuti Samueli anasankha ana ace kukhala oweruza. Mulungu sanawasankhe.

Ana a Samueli sanali monga atate ao. Iwo sanali kumvera Mulungu. Iwo anali oipa. Jowelo ndi Abija anayesa kugwiritsa nchito ofesi yao monga oweruza kupeza cuma. Iwo anali kulora kulipira cifukwa cocita kanthu kena koipa. Iwo anali kulamula anthu pofuna kudzikondweretsa okha.

Anthu Aisrayeli anakhumudwa. Akuru anapita kwa Samueli. Iwo anadziwa kuti Samueli acita bwino kwa iwo.

AKURU ANAPEMPHA MFUMU

Iwo anapereka zifukwa ziwiri zofunira mfumu. (1) Ana a Samueli anali oipa. (2) Mitundu ina yonse inali ndi mafumu.

Samueli sanali kufuna Mfumu. Iye anadziwa kuti Mulungu ndi mfumu ya Aisrayeli. Mulungu anafuna kulamulira anthu kupyolera mwa aneneri, ansembe, ndi oweruza. Anthu a Israyeli anali osakhulupirika kwa Mulungu. Samueli sanali okondwa ndi Aisrayeli.

MULUNGU ANAITANA MTSOGOLERI WATSOPANO

Mu 1 Samueli 1:1 kulefika 4:21, timawerenga za umoyo woyambirira wa Samueli. Samueli anali ndi moyo wokondweretsa pemene anali mnyamata. Makolo ace anamupereka kwa Mulungu. Anamupereka kukacisi kukakhala ndi Eli, wa nsembe. Iye usiku uli wonse anali kugona pafupi ndi likasa lamapangano.

Usiku wina, Samueli anamva mau akuitana dzina lace. Mulungu anamuuza kuti ana a Eli alangidwa cifukwa ca macimo ao. Eli anazindikira kuti Mulungu anali kuitana Samueli kuti amutumikire. Iye anaphunzitsa Samueli kukhala wa nsembe.

Mulungu anaitana Samueli kukhala Mneneri. Mneneri anali kupereka uthenga wa Mulungu kwa anthu. Ndipo iye anali kulankhulira anthu kwa Mulungu (1 Samueli 3:20-21).

Afilisti anali kulamulira Aisrayeli pa nthawi imeneyi. Iwo anagonjetsa Aisrayeli pankhondo yaikuru, kupha anthu zikwi zinai. Ndipo anaba likasa la mapangano. Mneneri wamkuru, Eli anafa pamene anamva kuti likasa labedwa (1 Samueli 4:17-18).

Samueli anakhala mtsogoleri watsopano wa Aisrayeli. Iye anadziwa kuti Israyeli ayenera kukhala waufulu kucokera kwa Afilisti. Ndi Mulungu yekha akanawakhazika kukhala aufulu Samueli anauza anthu kuti akhale okhulupirika kwa Mulungu. Iye anawauza kusiya kupembedza Baala ndi Asheroti. Iye anauza anthu kuti Mulungu adzawapatsa ufulu ndi cigonjetso. Koma Mulungu analamulira kuti





ANTHU MU UKAPOLO

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 1-2

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Eksodo 1:7-14

MAU APAMTIMA: "M'mozamamo ndinakupfuulirani Yehova. Ambuye imvani liu langa; makutu anu akhale cimverere mau a kupemba kwanga!"
Masalmo 130:1-2

Pa cisumbu cacing'ono ca Zanzibar pali gombe lalikuru la nyanja. Pa zaka zambiri za pitazo gombe limeneli anali kusungira akapolo oposa 500 azibambo ndi azimai amene anali kugulitsidwa mu ukapolo. Masiku ano gombeli limatikumbutsa momwe Afrika anabvutikira kucokera kukhalidwe loipa laukapolo. Ukapolo unali cinthu coipa. Unali kusiyanitsa ana ndi makolo. Unali kucotsa anthu pakati pa mtundu wao. Unakakamiza anthu kugwira nchito momangika.

Phunziro lino litiuza momwe Mulungu anathandizira Ahebri amene anali muukapolo. Ahebri anali anthu osankhulidwa a Mulungu. Mulungu anafuna kudalitsa dziko kupyolera mwa iwo.

(Tsopano Werengani Eksodo 1:7-14)

KUSINTHIKA M'NDALE

Poyamba, Aigupto anafuna Ahebri kuti akhale m'dziko lao. Farao anaitana Ahebri kudzakhala cifukwa ca Yosefe. Yosefe, mwini, poyamba anali kapolo. Abale ace ansanje ana-

mugulitsa kwa aluya opita ku Aigupto.

Mu Aigupto, Mulungu anadalitsa Yosefe ndipo anapatsidwa mpando waciwiri kwa mfumu Farao. Yosefe anasunga Aigupto ndi Ahebri kucokera ku mabvuto anjala yaikuru. Pamenepo Yosefe adafa. Farao amene anali kudziwa Yosefe anafanso. Mfumu yatsopano idalowa pampando. Ameneyu mwina anali Rameses II. Iye sanali kudziwa Yosefe (ndime 8).

Kawiri kawiri pokakhala kusintha pa ulamuliro, anthu amene anakondedwa amataya malo anchito zao. Cimeneci cidaonekera kwa Ahebri. Mfumu ya tsopano idaona kuti kunali Ahebri ambiri. Iye anali kuwaopa (ndime 9-10). Iye adaopa kuti Ahebri mu nthawi ya nkhondo akadakhoza kugwirizana ndi adani ndi kugonjetsa Aigupto.

Kodi Aigupto adaganizira kucita ciani kwa Ahebri?

(Werengani Eksodo 1:11-14 mokweza)

AHEBRI ANAKHALA AKAPOLO

Farao anapanga anthu aciHebri kukhala akapolo. Iye anali mtsogoleri wankhaza ndi olimbirira utsogoleri. Iye anafunitsitsa nchito ya akapolo kuti amange cifanizo cace ndi mizinda. Aigupto adapanga anthu a Mulungu kugwira nchito kwambiri. Iwo anamanga mizinda iwiri, Pitomu ndi Ramese (ndime 11).

Aigupto anayesetsa kupanga kuti agwire nchito yolimba kwambiri. Iwo anaganiza kuti kuwagwiritsa nchito kwambiri kukhoza kuononga



PHUNZIRO 13

TIPATSENI MFUMU

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Oweruza 21:25; 1 Samueli 8-10

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: 1 Samueli 8:1-9; 10:1

MAU APAMTIMA: "Ndipo ana a Israyeli anati kwa Samueli, Musaleke kutipempherera kwa Yehova Mulungu wathu, kuti Iye atipulumutse m'manja a Afilistiwo."
1 Samueli 7:8.

Maiko ambiri a ci Afilika anaganizira kukhala ndi mfumu. Kapena cifukwa cace ndi cakuti ufumu umakhalira kamodzi ndi kulamula mwa mphamvu ndikusowetsa mtendere.

Aisrayeli anapitiriza kudandaula kuti akhale ndi mfumu. Kodi muli kukumbuka muphunziro la mbuyoli kuti Aisrayeli anafuna kupanga Gideoni kuti akhale mfumu yao? Gideoni anakana. Iye anafuna Mulungu kuti akhale mfumu yao. Iye anadziwa zomwe anthu akanamacita pansi pa ulamuliro wa mfumu.

Pamene mtundu wa Aisrayeli unakula kukhala pfuko, anafuna atsogoleri. Mtundu uli wonse unadzilamulira okha. Mulungu anaitana oweruza kuti alamulire mitundu ngati cosowa citapezeka. Gideoni anali mtsogoleri wa gulu la nkhondo. Samsoni anatsogolera ndi mphamvu zace. Aliyense anali kucita zomwe anaganiza kuti ndi zabwino (Oweruza 21:25).

Samsoni anataya mphamvu yace pamene anacimwa. Pemphero ndi njira imene munthu amalankhula la Samsoni, ndi kumupatsanso mphamvu zace.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Cimo ndi malonjezo osweka zinaononga mphamvu ya Samsoni. Onani moyo wanu. Kodi cimo limasunga mphamvu ya Mulungu kunja kwa moyo wanu? Mulungu akhoza kukuthandizani kugonjetsa cimo ndikukhala moyo wa mphamvu. Bwanji osabvomereza macimo anu kwa Mulungu ndi kufuna cikululukiro cace. Lonjezani Mulungu kuti agwiritse nchito moyo wanu kuutumiki wace.

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Mulungu anapatsa Samsoni mphamvu zace. Mulungu amatipatsa mphamvu yocitira nchito yace.
2. Cimo linaononga moyo wa Samsoni. Linamulanda mphamvu ya Mulungu. Cimo likhoza kuononga miyoyo yathu ndikutilanda mphamvu ya Mulungu.
3. Samsoni anapempha Mulungu kuti amupatsenso mphamvu. Pamene ife tipempha kwa Mulungu, amatimvera. Iye adzatipatsa mphamvu zace ngati tikhala okhulupirika kwa iye.
4. Mulungu amafuna kuti anthu ace akhale okhulupirika kwa iye nthawi zonse.



umoyo wa Ahebri. Anaganizira kuti cimeneci cikadalepheretsa Ahebri kuti asakhale ndi ana ambiri. Komatu nthawi yokhwima siidaononge Ahebri. Iwo anali kuculukirabe. Dongosolo limeneli lidalephera. Farao adakonza njira ina yoonongera Ahebri.

Farao analamulira anamwino a ku Aigupto kuti adzipha ana acimuna onse aciHebri. Ana a akazi akhale ndi moyo. Koma anamwino anaopa Mulungu ndipo sanamvere. Anomwino anauza Farao kuti ana akazi ndiotiposa mphamvu ndipo anali kubeleka ife tisanafike. Ndipo Farao analamulira kuti ana a amuna onse aponyedwe mu mtsinje wa Nile (ndime 17 - 22). Inali nthawi yacisoni kwa Ahebri.

MPULUMUTSI WABADWA

Mutu waciwiri ufotokoza momwe Mulungu anagonjetsera Farao. Mulungu anali ndi dongosolo. Mose anali mbali ya dongosolo la Mulungu. Mkazi wa ci Hebri anabala mwana wa mwamuna. Maiyo anamubisa m'nyumba kwa miyezi itatu kuopa Aigupto. Patatha masikuwo sanakhoze kumubisanso m'nyumba. Motero adapanga kadengu kabango ndikugoneka mwana Mose m'menemo. Iye anaika kadenguko pakati pa bango lalitali kumapeto kwa mtsinje. Miriamu mlongo wa Mose, anali kudikilira kadenguko.

Tsiku lina mwana wa mkazi wa mfumu Farao anapita kumtsinje kukasamba. Iye anapeza kadengu. Iye anayang'ana mkati; ndipo pamene anaona kamwanako, anamva nako cifundo. Miriamu anafunsa ngati akadapeza wolera mwanayo. Ndipo anapita nakaitana mai wace wa Mose (ndime 6-10).

Amai a Mose anamusamalira nasungira mkazi wa mwana wa mfumu kufikira anakhala mnyamata. Ndipo anamutenga napita naye kunyumba ya mfumu. Mose anapita kusukulu yabwino koposa m'dziko. Iye anakulira m'nyumba mwa Farao ndipo anali kusungidwa monga mwana wa mfumu ya mu Aigupto.

Koma kodi ndi ciani cidacitika pamene Mose adakula?

(Werengani Eksodo 2:11-15 mokweza)

KUCOKERA KU UMWANA WA MFUMU KUKHALA - WOTHAWA THAWA

Tsiku lina Mose atangokula kukhala bambo, anaona munthu wa mu Aigupto alikumenya m'Hebri. M'hebri adaferatu. Mose adakumbukira kuti nayenso anali MuHebri. Iye sanakhoze kuiwala maphunziro amai wace. Mose anaunguza kufuna kuona ndani anali kumuona. Pamene iye sanaone aliyense, anapha mu Aigupto uja namubisa iye mu mchenga.

M'mawa wace Mose anaona Ahebri awiri alikumenyana. Iye anayesa kuletsa ndeu ija. Ahebri aja anafunsa Mose ngati afuna kuwapha monga anaphera mu Aigupto uja. Mose anacita mantha. Aliyense ayenera kudziwa kuti iye anapha munthu wa ci Aigupto! Mose anacita zoipa tsopano anali kucita mantha.

Farao anadziwa kuti Mose anapha m'modzi wa anthu ace. Iye anali okwiya nalamulira kuti Mose aphedwe. Mose anathawa mkwiyo wa Farao. Iye anathawira kudziko la Midyani kucipululu. Ndiye kuti mwana wa mfumu ndi mwai wa malo abwino anasandulika kukhala wothawa



Delila anali ndi munthu wometa tsitsi lace.

Mphamvu ya Samsoni siinali mu tsitsi lace. Koma tsitsi lace lalitali linali malonjezano osasweka akwa Mulungu. Pamene tsitsi lace lidametedwa, kumvana kwao pakati pa Samsoni ndi Mulungu kunaduka. Limodzi la ndime zocititsa cisoni mu Buku Lopatulika ndi Oweruza 16-20 "koma sanadziwa kuti Yehova adamcokera." Ndi cinthu cacisoni nthawi zonse pamene Mulungu asiya munthu yekha. Cimo ndi kusamvera kumapangitsa zimenezi.

(Werengani Oweruza 16:23-30 mokweza)

IMFA YA SAMSONI

Afilisti anakondwerera cifukwa cogonjetsa Samsoni. Iwo anapanga phwando lalikuru kwa Dagoni, milungu yao. Tsopano nkhondo siinali pakati pa Samsoni ndi Afilisti. Inali pakati pa Dagoni ndi Mulungu.

Afilisti ananena kuti Dagoni wapambana. Anathudzula maso a Samsoni kotero kuti asathe kuona.

Anabweretsa Samsoni kudzayesa woseweretsa ndikumuseka (ndime 26). Samsoni anapempha Mulungu kuti amubwezerenso mphamvu zace. Mulungu anamupatsa mphamvu zokwanira kuti akhonze kukoka ndi kugwetsa mizati ya nyumbayo. Afilisti zikwi zitatu anafa ndipo Samsoni anafanso.

Samsoni akhoza kutiphunzitsa ife phunziro lofunika koposa. Mulungu amatipatsa ife kulimbitsa ndi mphamvu zomutumikira iye. Koma cimo limasiyanitsa munthu kucokera kwa Mulungu.

lacinaziri. Anakhala umoyo waucimo. Anakwatira mkazi wacifilisiti.

Alamu a atate wa Samsoni anapereka mwana wace wa mkazi, mkazi wa Samsoni, kubwenzi la Samsoni. Samsoni anakalipa kwambiri. Anamangirira ankhandwe mazana atatu awiri awiri. Iye anaika miuni pakati pa micira. Ndipo anapitikitsira nkhanwezo m'minda ya Afilisiti. Minda inapsa yonse (Werengani Oweruza 15:4-5).

Afilisiti anakalipa kwambiri. Iwo anafuna kuononga Samsoni. Iwo anapha mkazi wosakhulupirika ndi atate ace (15:6).

Samsoni anapitirizabe kukhala moyo waucimo. Iye anagwiritsa mphamvu zace kuononga Afilisti. Iye anapha amuna zikwi ndi fupa la cigama ca bulu (15:15-16).

SAMSONI AKOMANA NDI DELILA

Samsoni anakomana ndi mkazi wokongola wochedwa Delila. Iye anali Mfilisiti. Afilisiti analipira ndalama kuti iye apeze za mphamvu ya Samsoni. Nthawi zitatu Samsoni anenena bodza kwa iye. Afilisti anadikira. Iwo anafuna kuononga Samsoni. Ndipo Delila anagwiritsa tsenga yakale pa Samsoni. Iye anamuuza kuti sanamukonde iye. Ngati akanamukonda iye, akanamuuza comwe cimamupatsa mphamvu. Delila anagwiritsa gulu la nkhondo ya Afilisti sakanacita. Iye anagwiritsa "cikondi" kufuna kunyenga Samsoni. Samsoni anamuuza kuti anali Mnaziri. Tsitsi lace linali losameta nthawi imeneyo. Mkaziyo anaitana nkhondo ya Afilisti. Samsoni anapita kukagona.



thawa.

Panthawi ya mkwiyo wa ciumunthu anadziona yekha kuti ndi M'Hebri ndikupha mu Aigupto.

Mose anakhala ku Midyani zaka makumi anai (40). Mulungu anali kumukonza kuti adzakhale mtsogoleri kutsogolo.

ZINTHU ZOYENERA KULINGALIRA

Anthu onse ali ndi nthawi yosautsa Mulungu amafuna kupatsa anthu ace mphamvu yopita nayo mu nthawi yamasautso. Mulungu amakonda anthu ace ndipo amabvutika nao pamodzi pamene ali kubvutika.

Pamene inu mukhala ndi nthawi yobvuta, Mulungu amasamalira. Iye adzakupangirani njira yakuti mucokemo. Iye adzayankha mapemphero anu monga momwe adayankha mapemphero a Ahebri. Kumbukirani kupempha Mulungu kuti akutsogolereni tsiku liri lonse.

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Aigupto anapanga Ahebri kukhala akapolo. Masiku ano anthu ndi akapolo a cimo. Anthu ndi akapolo a ndalama, zoledzeletsa, zobvala ndi zinthu zina.

2. Mulungu amafuna kupanga anthu kukhala aufulu. Iye amasamalira pamene tibvutika.

3. Pamene ife tipemphera kwa Mulungu, adzatithandiza kukhala mfulu kucoka ku macimo athu.

PHUNZIRO 2

## MTSOGOLERI AITANIDWA

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 3-4

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Eksodo 3:1-12

MAU APAMTIMA: "Ndipo Yehova anati, Ndapenyetsetsa mazunzo a anthu anga ali m'Aigupto, ndamvanso kulira kwao cifukwa ca akuwafulumiza; pakuti ndidziwa zowawitsa zao."
Eksodo 3:7

Atsogoleri ndi anthu ofunika koposa. Amathandiza kukongoletsa dziko lao. Atsogoleri abwino amayesa kucita zabwino zadziko lonse. Koma atsogoleri oipa kawiri kawiri amasokoneza ndikubvutitsa anthu amudziko lao. Idi Amin anali mtsogolri woipa. Iye anapha anthu ambiri ndi kulamulira dziko lace la Uganda ndi mantha ndi ciopsezo.

Anthu amafuna atsogoleri. Kunyoza ndi cisokonezo cimaoneka ngati anthu asoweka utsogoleri. Pamene Ahebri anali kukhala mu Aigupto analibe mtsogoleri cifukwa anali akapolo. Koma, Mulungu anadziwa kuti adzafunika mtsogoleri atakhala aufulu. Kodi Mulungu adapeza mtsogoleri wa Ahebri motani?

(Werengani Eksodo 3:1-12 mokweza)

MULUNGU ALANKHULA KWA MOSE

Mose anathawa kucoka ku Aigupto cifukwa Farao anafuna kumupha. Iye adapita ku Midyani



Nthano ya Samsoni ili mu Oweruza 13-16.

(Werengani Oweruza 13:1; 16:23-30 mokweza)

KUBADWA KWA SAMSONI

Manowa ndi mkazi wace analibe ana. Tsiku lina mngelo anabwera ndi uthenga kucokera kwa Mulungu. Mulungu adzawapatsa mwana wa mwamuna.

Manowa ndi mkazi wace anali kufuna mwana kwambiri. Mngelo anawauza kuti mwana wao adzakhala osiyana. Adzakhala m'naziri. Mnaziri anali munthu opatulidwa ndi woperekedwa kwa Mulungu. Iye anayenera kulumbira malonjezo aunaziri. (Onani Numeri 6). M'naziri sakanamamwa vinyo kapena zoledzeletsa. Iye sakanamadya mphesa kapena zipatso zina. Iye sakanameta tsitsi lace. Mnaziri sakanamakhudza cinthu cakufa.

Manowa ndi mkazi wace anapemphera kuti Mulungu adzawapange kukhala makolo anzeru (13:8). Samsoni anakula mwamsanga. Anakula nakhala wamkuru. Mzimu wa Mulungu anali pa Samsoni. (Oweruza 13:24-25) Mulungu anapatsa Samsoni mphamvu zazikuru.

MOYO WA SAMSONI

Mulungu anasankha Samsoni kukhala Oweruza wa Aisrayeli. Iye anali mtsogoleri wankhondo. Samsoni anali oyenera kugonjetsa Afilisiti. Analamulira pa Aisrayeli kupambana zaka makumi anai (13:1).

Samsoni sanamvere Mulungu. Iye anadalira pa mphamvu zace za iye yekha. Anapwanya lamulo

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Inu mukhoza kukhala mtsogoleri wolimba wa Mulungu, monga momwe Gideoni analiri kwa Aisrayeli.

2. Tiyenera kutsata dongosolo la Mulungu la za miyoyo yathu kukhala mtsogoleri olimba mtima. Mulungu ali ndi dongosolo ndi munthu aliyense.

3. Mabvuto amafika pamene tiiwala Mulungu.

PHUNZIRO 12

## KULIMBANA NDI OTSUTSANA

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Oweruza 13-16

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Oweruza 13:1; 16:23-30

MAU APAMTIMA: "Yehova ndiye kuunika kwanga ndi cipulumutso canga; ndidzaopa yani? Yehova ndiye mphamvu ya moyo wanga, ndidzacita mantha ndi yani?"
Masalmo 27:1

Zaka zambiri zapitazo, Filbert Bayi, waku Tanzania, anacita masera aliwiro athupi ndi mphamvu. Iye anathyola citsulo ca 1,500 comwe mbiri yace inamveka kudziko lonse.

Phunziro limeneli ndi lamunthu amene ali ndi mphamvu zathupi. Dzina lace ndi Samsoni



ca kum'mawa kwa Aigupto. Mose anakhala ku Midyani kwa zaka makumi anayi (40). Iye anakhala osamalira nkhosa za wa nsembe Jetero wa ku Midyani. Iye adakwatira Zipora, m'modzi wa mwana wa Jetero, ndipo anali kukhala mokondwa ku Midyani kwa zaka makumi anayi. Ndipo tsiku lina mtima wace wa mtendere wawoweta ziweto unatha. Mulungu adalankhula kwa Mose. Iye anamuitana kuti akhale mtsogoleri wa anthu aci Hebri.

Mulungu adalankhula kwa Mose kupyolera mucitsamba coyaka. Mose anaona citsamba cikuyaka, koma osapselera. Pamene Mose anaima kuti aone cinthu codabwitsaco, Mulungu anati, "Mose, Mose" (ndime 4).

Mose anaima pamalo oyera, pamaso pa Mulungu mwini weni weni. Motero Mose anabvula nsapato zace, poonetsa ulemu ndi cibvumbulutso ca Mulungu. Ifenso tiyenera kuima mwaulemu ndi kuwerama mwacibvumbulutso pamaso pace.

Tsopano Mose sanadziwe Mulungu bwino. Motero Mulungu anadzibvumbulutsa yekha kwa Mose. Iye anali Mulungu wa makolo a Mose, Mulungu wa Abrahamu, Isake ndi Yakobo. Ndipo Mose anazindikira kuti Mulungu anali yani. Iye anacita mantha nabisa nkhope yace. Iye anacita mantha kuyang'ana kwa Mulungu (ndime 6).

Mulungu anaonetsa Mose kudziwa kuti Iye asamalira anthu ace. Mulungu anali ndi nchito ya kuti Mose aicite.

## MULUNGU ANASAMALIRA ANTHU ACE

Mulungu anauza Mose kuti iye anadziwa kuti Ahebri anali kubvutika ndi kuti iye adzapulumutsa anthu ace (ndime 7-8). Iye anauza Mose kuti adzalowetsa Ahebri mu dziko "la mkaka ndi uci." (ndime 8).

Dziko lamalonjezanoli ndi lolemera. Linali ndi zakudya zambiri. Ngakhale kuti anthu ena anali kukhala mu dziko lamalonjezano pa nthawi imeneyo, Mulungu anafuna kulipanga likhale dziko la Ahebri.

## MULUNGU APATSA MOSE NCHITO YOCITA

Mulungu anati kwa Mose, "Tiye tsopano ndikutuma kwa Farao, kuti uturutse anthu anga ana Aisrayeli m'Aigupto." (ndime 10).

Kodi mukhoza kuganizira yankho ya Mose ku mau amenewa? Mose anathawa kucoka kwa Farao cifukwa anafuna kumupha iye. Tsopano Mulungu anafuna kuti iye abwerere ku Aigupto ndikukatsogolera anthu ace kucokera muukapolo.

Mose anali okaika cifukwa ca luntha lace. Mu ndime yakhumi ndi cimodzi, Mose anafunsa Mulungu, "ndine yani ine kuti ndipite kwa Farao, ndi kuti nditurutse ana Airayeli m'Aigupto?" Kodi munthu yemwe siali kanthu angatulutse motani anthu a Mulungu muukapolo? Mose mwina anaganiza kuti Ahebri sadzamumvera. Iye anadziwa kuti Farao sadzamumvera. Koma, zoonadi Mulungu anadziwa zonse za Mose ndi momwe angalekezere zinthu, komabe Mulungu ananena kuti anafuna Mose kuti apite, ku Aigupto. Mulungu sanali kutuma Mose yekha.



Cigonjetso sicingathe kufotokozedwa, koma kungonena kuti cinali cocokera mu mphamvu ya Mulungu.

Anthu anali okondwa (Oweruza 8). Kodi anafuna kucita ciani?

## GIDEONI SAKADAKHALA MFUMU

Aisrayeli anafuna kupanga Gideone kuti akhale mfumu yao. Gideoni anati ai. Werengani ndime yapamtima kaciwiri. Gideoni anati kapena iye kaya ana ace sadzakhala mfumu. Mulungu ndiye mfumu imene Aisrayeli angaifune.

Gideoni anapempha anthu kuti abweretse golide kuti apange mkanjo wa oferi. Oferi unali mkanjo woperekera nsembe. Gideoni anacita mkanjowu kufuna kukumbutsa anthu za cigonjetso cimene Mulungu anawapatsa. Koma posacedwa unasanduka kafano. Anthu anaiwala Mulungu nayamba kupembedza Oferi (Oweruza 8:27).

Gideoni anali mtsogoleri wa mphamvu. Komabe cikoka comwe anali naco pa Aisrayeli sicinapitilire. Pamene Gideoni anafa, anthu anabwerereranso kwa Baala (Oweruza 8:33).

## ZINTHU ZOLINGALIRA

Kodi inu ndinu Gideoni watsopano oonetsa kulimba mtima mu cikhulupiriro canu? Mulungu adzatipatsa ife kulimba mtima kuti tigwire nchito yace. Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kukhala olimba mtima kuti mulankhule za iye.

Gideoni kutumiza kumudzi onse anali kucita mantha! Pamene iye anatsata dongosolo la Mulungu, iye anali ndi ankhondo zikwi zitatu otsala!

Nthawi zina timaganiza kuti mphamvu ziri mukucuruka kwa anthu. Ndipo tikhoza kuganiza kuti ndiye "mpingo wamphamvu" kutanthauza mpingo umene uli ndi anthu ambiri. Buku Lopatulika silibvomerezana ndi mau amenewa. "Ndi mphamvu ai, koma ndi Mzimu wanga, ati Yehova wa makamu" (Zakariya 4:6).

Mulungu anafuna Aisrayeli kudziwa kuti iye ndiye anawapatsa cigonjetso. Pamene ife tifika pacolinga kapena kupambana ndi cigonjetso, Mulungu amatithandiza. Ife sitimapambana ndi mphamvu zathu.

Gideoni anakonza gulu la nkhondo ndi thandizo la Mulungu.

(Werengani Oweruza 7:20-21 mokweza)

MULUNGU ANAPEREKA CIGONJETSO

Nkhondo ya Gideoni ya anthu mazana atatu inazungulira cigono ca Amidiyani. Zida zao zinali mbiya za dothi ndi malipenga (ndime 20). Ankhondo a ci Hebri anamenya nkhondo pogwira muuni woyaka, kuimba malipenga, ndi kuswa mbiya za dothi! Amidiyani anacita mantha ndipo anathawa! Iwo sanayese kuteteza mzinda. Iwo anathawa!

Mulungu akhoza kucita zinthu zonwe. Aisrayeli anagonjetsa opanda zida. Ankhondo ya Amidiyani anali ambiri kuposa wa Aisrayeli, koma Mulungu anapatsa Aisrayeli cigonjetso.



Mulungu anadzipereka kuti athandiza Mose.

MULUNGU ADZIPEREKA KUTHANDIZA MOSE

Mulungu anauza Mose kuti sadzakhala yekha. Mulungu analonjeza kuti adzatulutsa Ahebri kucoka mdziko la Aigupto kufika "kuphiri limeneli." Phiri limeneli linali phiri la Horebi kapena phiri la Sinai. Mulungu analankhula kwa Mose ku nthawi yoyamba pa phiri limeneli ndipo nthawi ina anamupatsa malamulo kumeneko.

Sizinali kanthu kwa Mulungu kuti Mose anali yani. Iye sanasamale kuti Mose anali mu Israyeli wophunzitsidwa ngati m'Aigupto. Iye sanasamale kuti anali kucipululu mbusa wophunzitsidwa ndi wa nsembe. Anthu amakonda kunena za maphunziro ndi kudziwa kwa nchito, koma Mulungu anangoti, "ndidzakhala ndi iwe," (ndime 12).

MULUNGU AITANA ANTHU MASIKU ANO

Mulungu amadziwa zakubvutika kwathu ndizosautsa. Iye amamvetsetsa mabvuto athu. Mulungu samaiwala anthu ace. Iye adzatithandiza masiku ano monga momwe anathandizira Ahebri.

Mulungu amaitana anthu munjira zambiri. Iye akhoza kugwiritsa nchito citsamba coyaka, mlendo kapena njira ina. Pali nthawi zonse dongosolo la ciyero cobisika cocitika poitana mtsogoleri. Komabe Mulungu amagwiritsa nchito anthu wamba amene amabvomereza kukuitana kwace kudzacita zinthu zazikuru. Kodi Mulungu alikuitana inu kuti mucite kanthu kena? Zoonadi iye ali ndi nchito yanu ndi yanga. Ndipo tikhoza kukhala otsimikiza za kupezeka ndi

cithandizo cace.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Kuli mabvuto ambiri m'dziko la masiku ano. Ngati wina ayang'ana pa nyuzi pepala, wina akhoza kuwerenga za cigumula, njala, kuphwanyika ndi zinthu zina zoopsa. Mkristu ayenera kuona zinthu zimenezi monga mwayi wothandiza anthu omwe ali mu zosowa.

Tiyeni tione anthu ndi maso "acithandizo." Pempherani kuti Mulungu akutsogolereni kumalo komwe inu mukhoza kuthandiza munthu wina wace.

ZOMWE PHUNZIRORI LIKUTIPHUNZITSA

1. Mulungu nthawi zonse amasamalira anthu ace. Iye amatumiza anthu monga Mose kukawathandiza.

2. Mulungu amaitana anthu kuti akatsogolere anthu ace. Munthu ndi wosayenera kapena wokhoza kucita nchito yekha.

3. Mulungu adalonjeza kutithandiza pa nchito ili yonse imene amatipatsa kuti tiicite. Ndi mphamvu ya Mulungu tidzapambana.



Mulungu analankhula kwa Gideoni ndi kumuitana iye kuti atsogolere Aisrayeli. Werengani momwe Gideoni molimba mtima analankhulira m'malo mwa Mulungu ndikulowa mu umunthu weni weni.

(Werengani Oweruza 6:11-24 mokweza)

MULUNGU APATSA AISRAYELI MTSOGOLERI

"Mngelo" analankhula kwa Gideoni. Mulungu anaitana Gideoni kuti akatsogolere anthu kuti akamenyane ndi Midiyani. Mulungu anauza Gideoni kuti aononge guwa la Baala lomwe lidamangidwa ndi atate a Gideoni.

Anthu anakalipa. Iwo anafuna kupha Gideoni cifukwa iye anaononga guwa. Yoasi, atate a Gideoni, anachinjiriza Gideoni.

Gideoni anafuna kudziwa kuti Mulungu adzakhala ndi iye, ngati amenyana ndi Amidiyani. Iye adapempha Mulungu cizindikiro.

(Werengani Oweruza 7:2-8, 20-21 mokweza)

GIDEONI ASANKHA ANKHONDO

Gideoni anaitana anthu kukhala ankhondo (Oweruza 6:34). Anthu zikwi makumi awiri mphambu ziwiri anayankha kuitana kwa Gideoni (Oweruza 7:3). Kodi Gideoni anacita ciani pofuna anthu kuti akonzekere nkhondo?

Mulungu anauza Gideoni kuti anali ndi ankhondo ambiri! Aisrayeli akadakhoza kuganizira kuti anapambana cifukwa anali ndi gulu lalikuru la ankhondo! Motero Mulungu anauza

Timalora cimo kuti liononge ciyanjano cathu ndi Mulungu.

3. Aisrayeli anapanga lonjezano latsopano pa Sekemu, tiyenera kupereka miyoyo yathu kwa Mulungu monga momwe Aisrayeli anacitira pa Sekemu.

4. Mulungu amafuna anthu ace kukhala okhulupirika kwa Iye.

PHUNZIRO 11

GIDEONI: MUNTHU WA MULUNGU WOLIMBA MTIMA

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Oweruza 6-8

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Oweruza 7:2-8, 20-21

MAU APAMTIMA: "Koma Gideoni ananena nao. Sindidzalamulira inu, ngakhale mwana wanga sadzalamulira inu, Yehova adzalamulira inu."
Oweruza 8:23

Mu Afilika muli mitundu ina yomwe ili ndi miyambo yomwe imatsimikiza kuti munthu wafika pa umunthu. Masiku akale a Masaai anali kupha mkango kufuna kuonetsa kuti munthu wafika pa msinkhu wa umunthu. Miyambo imeneyi inali kuonetsa pa msinkhu wakulimba mtima wa munthu.

Phunziro la lero ndi la za Oweruza m'modzi wa Aisrayeli. Dzina lace anali Gideoni. Iye anadziwika cifukwa ca kulimba mtima wace.



PHUNZIRO 3

LOLANI ANTHU ANGA APITE

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 5-14

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Eksodo 5:1,11-13

MAU APAMTIMA: "Ndipo Mose ananena ndi anthu, musaope, cirimikani, ndipo penyani cipulumutso ca Yehova, cimene adzakucitirani lero."
Eksodo 14:13

Kwa zaka zambiri anthu aku Zimbabwe analirira ufulu wa ndale. Pakati pa usiku wa April 17, 1980, cimeneci cinakwaniritsidwa. Mbendera ya ci British inatsitsidwa ndipo aliyense anakweza mau mokondwera pamene mbendera ya ku Zimbabwe inali kukwezedwa. Zimbabwe anali waufulu.

Anthu onse amafuna kukhala omasuka kucokera ku ukapolo. Koma kawiri kawiri ulendo wa nkhondo ya ufulu ndi wautali ndi woopsa. Ufulu wa kumasuka kwa Ahebri siunali wapafupi. Muphunziro lathali taona momwe Mulungu adalamulira Mose cifukwa ca nchito ya ufulu. Mose adapanga ulendo wofulumira kucokera ku Midyani kupita ku Aigupto. Aroni, mbale wa Mose anapita naye monga olankhulira mmalo mwace. Pamene Mose anafika ku Aigupto, anasonkhanitsa atsogoleri a Aisrayeli kuwafotokozera uthenga ndi dongosolo lace.

KUTSIMIKIZA UTSOGORERI WACE

Sicinali capafupi kwa Mose kuti agonjetse Aisrayeli ndi utsogoleri wace. Iye anali

mlendo kwa iwo. Komabe anafunika kuti akapolo amenewa amukhulupirire ngati iye akadayenera kuwatsogolera kuufulu. Anthu obvutika amakaika ndi anthu akudza. Mose adayenera kudzionetsera kwa iwo ndikuwapempha kuti amutsate. Mu Eksodo 4:31, tiphunzira kuti iye anapambana pakuti, "anthu anamukhulupirira... ndipo anawerama mitu yao pansi ndikupembedza." Farao anali yemwe Mose anafuna kukamuona.

MOSE ATSIMIKIZIRA FARAO

Mose ndi Aroni anapitanso kwa Farao ndikukamuuza kuti Mulungu akuti, "Lola anthu anga apite" (Eksodo 6:11). Mulungu anati adzalanga Aigupto ngati Farao akaniza Ahebri kuti apite.

Mulungu analanga Aigupto powatumizira milili isanu ndi inai pa iwo (Eksodo 7:17 - 10:29). Pa nthawi ya mulili uli wonse Farao anali kulonjeza kuti amasula Ahebri. Mulungu akaletsa mulili koma Farao sanali kukwaniritsa malonjezano ace.

(Werengani Eksodo 11:1-6; 13:17-22 mokweza)

MULILI WA IMFA

Mose anauza Farao za mulili wa imfwa koma Farao sanalora kuti Ahebri apite. Mulungu anauza Mose momwe angapulumutsire Ahebri kucokera ku imfa. Eksodo 12 mu Buku Lopatulika lanu limatiuza za zimenezi. Cimeneci cinali ciyambi ca phwando la paska. Linali tsiku loyamba la chuthi ca phwando la Ayuda.

Banja la ci Hebri liri lonse lidayenera kupereka nsembe ya mwana wa nkhosa ndi kuika



rika kwa Mulungu.

Yoswa analemba pangano. Cinali monga mapangano apakati pa mitundu iwiri. Yoswa anawauza kuti Mulungu adzawalanga ngati sadzakhala okhulupirika kwa iye. Mulungu yonse iyenera kucotsedwa.

Mwala waukulu omwe unaikidwa pa Sekemu unakumbutsa anthu zalonjezano lomwe anapanga ndi Mulungu. Sekemu anali malo ofunika kwambiri. Mulungu analonjeza dziko la malonjezano kwa Abrahamu ku Sekemu. Thupi la Yosefe linaikidwa m'manda kumeneko. Tsopano Mulungu anapangana pangano latsopano ndi Aisrayeli kumeneko. Mwala waukulu udzakumbutsa anthu za mapangano. Udzawakumbutsa kuti akhale okhulupirika kwa Mulungu wa atate ao.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Ganizirani za moyo wanu. Kodi cimo limakulephweretsani kutumikira Mulungu. Kodi mufunika kudziperekanso kwatsopano kwa Mulungu? Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni mu utumiki wanu wotumikira iye tsiku ndi tsiku.

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Aisrayeli anali wosakhulupirika kwa Mulungu. Mulungu anagwiritsa Yoswa kuwaitana iwo kuti adzipereke kwa Mulungu mwa tsopano. Mulungu wakhala akugwiritsa nchito anthu nthawi yaitali kukumbutsa anthu za kudzipereka kwao kwa iye.

2. Kawiri kawiri Akristu sakhala okhulupirika. Timaiwala za udindo wathu wa Cikristu.

kira Mulungu. Anthu ena amapanga mulungu wa zokondweretsa kapena nchito kapena zinthu zina.

Yoswa anaikira citsanzo Aisrayeli comwe akadacitsata. Iye anati, "koma kwa ine ndi apabanja langa, tidzatumikira Mulungu" (ndime 15).

Pamene mtsogoleri atenga mbali ya coonadi, anthu ambiri adzatsata. Tisoweka atsogoleri monga Yoswa. Tisoweka anthu amene angaitane ife kuti tibwerere kwa Mulungu.

AISRAYELI ANADZIPEREKA OKHA KWA MULUNGU

Anthu a Mulungu anati atsata citsanzo ca Yoswa. Iwo analonjeza kutumikira Mulungu. Analonjeza kucotsa milungu yonama yonse kunja kwa miyoyo yao. Iwo anakumbukira madalitso onse omwe Mulungu anawapatsa.

Tisoweka kukonzanso kudzipereka kwathu kwa Mulungu nthawi zambiri. Tisoweka citsitsimutso monga Aisrayeli. Timaiwala kuti tisoweka Mulungu. Nthawi zambiri timafunika citsitsimutso mu miyoyo yathu. Timafunika citsitsimutso pamene tisiya kupemphera ndi kuwerenga mau a Mulungu. Tifunika citsitsimutso popemphera kwa Mulungu kuli kofunika kwa ife. Aisrayeli anapanga pangano lao latsopano ku Sekemu.

ANTHU APANGA LONJEZANO KU SEKEMU

Anthu analonjeza kutumikira Mulungu. Yoswa anawauza kuti adzaona kuti ndi zobvuta (ndime 19). Anthu analonjeza kukhala okhulupi-



mwazi wa nsembe ya nkhosayo pa mphuthu ya khoma. Mulungu adapulumutsa ana ao monga analonjezera.

Koma imfa inafika m'nyumba za Aigupto usiku. Mwana woyamba kubadwa wa mabanja onse wa Aigupto anaphedwa. Farao anaitana Mose ndi Aroni. Iye anawauza kuti atulutse Ahebri kucoka mu Aigupto mwamsanga momwe angathere.

MULUNGU ATSOGOLERA AHEBRI POTULUKA MU AIGUPTO

Eksodo 13:17-22 amafotokoza momwe Mulungu anatsogolera anthu potuluka mu Aigupto. Njira yacidule yakudziko lamalonjezano inali yodzera kugombe. Afilisiti anali kukhala mumbali mwagombe ndipo anthu ambiri anali kudzera njira imeneyo.

Anthu aci Hebri anali asanaphunzitsidwe kumenya nkhondo. Motero Mulungu anawatsogolera njira ina. Mulungu anatsogolera anthu mazana asanu ndi limodzi, kuphatikiza azimai ndi ana, kudzera ku cipululu. Aisrayeli anakhala mu Aigupto kwa zaka 430. Mulungu anakonzekera kuti anthu ace apitenso ku Kenani. Motero Mulungu anawatsogolera "usana ndi mtambo, njo... ndi usiku ndi moto njo" (Eksodo 13:21).

Yosefe anauza Aisrayeli kuti adzacoka mu Aigupto. Iye anawapempha kuti adzatenga mafupa ace ndi kupita nao kudziko lace (Genesis 50:24-25). Mose anacita monga Yosefe anafunira.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Nthawi zonse Mulungu amasamala anthu ace. Iye amafuna anthu masiku ano kukhala aufulu kucokera ku cilango ca cimo. Aigupto sanali kumvera Mulungu ndipo anasauka ndi cilango. Aisrayeli anamvera Mulungu ndipo iye anawapulumutsa kucokera ku ukapolo. Yesu amafuna kuti inu muthandize ena kukhala aufulu ku ucimo.

ZIMENE PHUNZIROLI LITIPHUNZITSA

1. Mulungu akhoza kugonjetsa mphamvu zoipa ndi zopsinja. Iye anagonjetsa Farao ndipo amagonjetsa zoipa masiku ano. Tsogolo liri m'manja mwace.

2. Mulungu amagwiritsa nchito anthu pofuna kuombola opsinjika. Iye anagwiritsa nchito Mose pothandiza Aisrayeli. Aliyense wa iye ali ndi mbali mu dongosolo la ciombolo ca Mulungu.

3. Mulungu adzalanga anthu amene samumvera iye, monga momwe analangira Aigupto.

4. Mulungu adzatipatsa kukhala aufulu kucokera ku cilango ca cimo, ngati tikhulupirira Yesu kuti atipulumutse ife.



Tisoweka kukumbutsidwa za udindo wathu wa kwa Mulungu. Tifunika kudzipereka mwa tsopano pomutumikira iye.

Aisrayeli anali kupembedza Mulungu kwa nthawi yocepa ndipo anali kutsata njira ina. Yoswa anayesa kuitana anthu kuti abwererenso kwa Mulungu. Iye anali munthu wokalamba kwambiri. Yoswa anakumbutsa anthu za madalitso a Mulungu akwa iwo.

Mu Yoswa 24:1-13, timapeza za nthano ya momwe Mulungu anatsogolera ndi kudalitsa Aisrayeli. Ndipo anauza anthu kuti alape ndi kupanga pangano latsopano kwa Mulungu m'modzi woona.

(Tsopano werengani Yoswa 24:14-15, 19-28)

YOSWA APEMPHA KUDZIPEREKANSO KWA TSOPANO

Yoswa anati Aisrayeli anayenera "kuopa Ambuye" (ndime 14). Iye sanatanthaunze kuti adzicita mantha. Iye anatanthauza kuti ayenera kudalira mwa Mulungu. Iwo adayenera kuzindikira mphamvu ya Mulungu. Yoswa anadziwa kuti Aisrayeli ena anali kupembedza kuti Aisrayeli ena anali kupembedza milungu ina. Iye anawauza kuti "acotse" milungu imeneyi (ndime 14). Mulungu sangakhale mwa ife ngati tiri ndi milungu ina.
Mulungu anaitana pa anthu kudziganizira. "Sankhani yemwe mudzamutumikira" (ndime 15). Iwo akadasankha milungu yonama kapena akadasankha Mulungu. Iwo sakadatha kupembedza onsewo.

Ife tiribe milungu yonama monga Baala. Komabe, milungu yambiri imatilepheretsa kutumi-

## KUKONZANSO PANGANO

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Deuteronomo 26; Yoswa 24.

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Yoswa 24:14-15, 19-28

MAU APAMTIMA: "Ndipo ngati kutumikira Yehova kukuipirani mudzisankhire lero amene mudzamtumikira, kapena milungu imene anaitumikira makolo anu okhala tsidya lija la mtsinje, kapena milungu ya Aamori amene mukhala m'dziko lao; koma ine, ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikira Yehova."
Yoswa 24:15

Muphunziro lotsiliza tinaphunzira za mabvuto omwe Aisrayeli anali nao posunga pangano lao ndi Mulungu. Aisrayeli anadzipereka okha kumayesero kuti apembedze milungu ina. Mulungu anapitiriza kuwaitana kuti abwerenso kwa iye. Phunziro la lero litiuza momwe Mulungu anagwiritsa munthu kuti akonzenso pangano. Iye anagwiritsa Yoswa kuti aitanenso anthu kuti abwerere kwa iye.

Phunziro la kukonzanso, kapena citsitsimunso, ndi yopanda nthawi ya kwa mitundu yonse. Kodi mumayamba mwaima mu moyo wanu wa tsiku ndi tsiku ndi kuperekanso moyo wanu kwa Mulungu? Kodi mumamva monga mtumwi Paulo amene anati, "Sinditha kucita zabwino zomwe ndifuna kucita, m'malo mwace, ndimacita coipa comwe sindicifuna!"





## MADYERERO AUFULU

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Eksodo 14 - 15

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Eksodo 14:21-25, 30-31; 15:1-3, 20-21

MAU APAMTIMA: "Afanana ndi Inu ndani mwa milungu, Yehova? Afanana ndi Inu ndani, wolemekezedwa, woyera, woopsa pomyamika, wakucita zozizwa?"
Eksodo 15:11

Caka ndi caka maiko anu Afilika amakhala ndi cikondwerero pa masiku omwe anapata ufulu wao. Pacikondwerero cimeneci pamakhala nyimbo, kubvina ndi zolankhula zambiri. Limakhala tsiku la chuthi, ndi lokondweretsa. Anthu a Mulungu nao anali ndi nthawi yapadera yokondwerera ufulu woturuka mu Aigupto. Kodi cidaoneka ndi ciani kwa Aisrayeli pamene anaturuka mu Aigupto?

(Werengani Eksodo 14:1-20 mokweza)

### AIGUPTO ALONDOLA AHEBRI

Pamene Ahebri anangoyamba kuyenda kulowa mu cipululu Farao anasinthanso maganizo ace. Iye ana zindikira kuti anataya akapolo ace. Kodi ndi ndani adzagwira nchito yonse yolimba? Motero iye anaitana gulu lankhondo kuti athamangire Ahebri. Iwo anatenga zobvala zao za nkhondo ndi magaleta kuti akagwire Ahebri pa nyanja yofiila. Ahebri anali kucita mantha kwambiri. Iwo analakalaka kubwerera ku Aigupto komwe (ndime 10-12).

Mose anali ndi cikhulupiriro. Iye anadziwa kuti Mulungu sangawasiye iwo. Mulungu anauza Mose kuti adzipitabe mtsogolo. Nyanja yofiila inali kutsogolo kwa Ahebri, ndipo gulu la nkhondo la Aigupto linali pambuyo pao! Mulungu analonjeza cigonjetso kupambana Aigupto. Koma motani? Werengani Eksodo 14:21-25,30-31. Kodi ndi codabwitsa cotani comwe Mulungu anacipanga?

KUOLOKA NYANJA YOFIILA

Zindikirani kuti Mulungu anacita zodabwitsa. Ahebri anali kuopa ndipo analibe malo ena aufulu opitako. Ndipo mphepo inafika ndipo madzi anagawika. Zipupa za madzi zinacinjiriza Ahebri pamene anali kuoloka nyanja yofiila mwaufulu. Koma, Aigupto anali kuwatsatabe.

Motero Mulungu anauza Mose zoyenera kucita, pamene Ahebri onse anali tsidya lina la nyanja, Mose anatambasula manja ace. Madzi anakomana. Aigupto, azibambo, akabvalo, ndi magaleta, zinamira m'madzi. Onse anafa. Ambuye anali opambana ndikugonjetsa Aigupto.

(Werengani Eksodo 14:30-31, 15:1-3,20-21 mokweza)

CIPULUMUTSO NDI NYIMBO

Ambuye anapulumutsa Aisrayeli kucokera kwa Aigupto tsiku limenelo. Ahebri anaona Aigupto akufa atagona pa gombe la nyanja. Cigonjetsoco cidawapatsa cikhulupiriro catsopano mwa Mulungu. Iwo anaona codabwitsa cace cacikuru.



ndi nchito ikhoza kukhala mulungu kwa ife. Pamene titumikira milungu yonama monga imeneyi, nthawi zonse timalephera. Timalephera kulandira madalitso omwe Mulungu anafuna kutipatsa. Cimo limationonga ife. Tiyenera kuika Mulungu kukhala oyamba mu miyoyo yathu.

ZINTHU ZOGANIZIRA

Ganizirani za milungu yonama m'dziko lathu. Kodi ndinu wotsutsika cifukwa cotumikira milungu yonama? Pamene cinthu cikhala cofunika kwambiri kuti palibe cina codetsa nkhawa, ndiye kuti kanthuko kakhala mulungu. Mulungu akhoza kukuthandizani kucotsa milungu yonama m'moyo wanu.

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Aisrayeli posacedwa anaiwala Mulungu wa atate ao, amene anawapatsa dziko la malonjezano. Iwo anayamba kupembedza milungu ya anthu omwe anali nao pafupi.

2. Ife tiri ndi milungu yonama m'dziko lathu masiku ano. Mulungu wonama ndi cinthu ciri conse comwe cimatilepheretsa kutumikira Mulungu.

3. Aisrayeli anali wosatetezedwa kwa adani ao, wopanda Mulungu. Mulungu amatiteteza kucokera kuzoipa za dziko lathu.

4. Mulungu sakhala okondwera pamene ife sindife okhulupirika kwa iye.

## MULUNGU ANAKALIPIRA AISRAYELI

Mulungu ndi woyera. Cifukwa ca cimeneci, sangalekerere cimo. Iye amadziwa pamene anthu acimwa. Mulungu anakalipira anthu ace.

Aisrayeli anasiya Mulungu. Mulungunso anawasiya. Adani anayamba kuwagonjetsa. Iwo anayamba kulandidwa dziko la malonjezano lomwe Mulungu anawapatsa (ndime 15). Mulungu anakalipa, koma iye nthawi zonse amafunitsitsa kupulumutsa anthu. Werengani ndime 17 kuti muphunzire za dongosolo la Mulungu.

(Werengani Oweruza 2:17 mokweza)

## MULUNGU ASANKHA OWERUZA

Mulungu analanga anthu cifukwa ca macimo ao. Iye anapatsa Aisrayeli oweruza. Anthuwo anali asilikali. Anatsogolera Aisrayeli kuti apambanenso. Anatsogolera boma.

Oweruza anatsogolera anthu. Aisrayeli anawatsata kwa kanthawi pang'ono. Koma "anatembenuka mwamsanga" (ndime 17) kubwerera ku milungu yonama. Mbadwo uli wonse unalowerera m'macimo (ndime 19).

Motero Mulungu anakwiya koposa. Iye anauza anthu iye sadzathandiza Aisrayeli kucotsa adani ao. Anthu sanali kulapa kweni kweni.

Ifetu tiribe milungu monga Baala ndi Asitaroti. Koma ngati tiika ciri conse m'malo a Mulungu kanthu kameneko ndi Mulungu kwa ife. Ndalama, zoledzeletsa, zosangalatsa



Iwo anadalira mwa Mulungu kwambiri, ndipo anali ndi cikhulupiriro cacikuru mwa Mose, mtsogoleri wa Mulungu. Iwo sanali kudandaulanso ndi kunyinyilika. Anthu anabvomereza ku mphamvu ya cozizwitsa poimba nyimbo zoyamika ndi zothokoza. Cikhulupiriro mwa Mulungu ndi cikhulupiriro ca nyimbo.

Muli nyimbo zacigonjetso ziwiri mu Eksodo 15. Nyimbo ya Mose ipezeka mu ndime 1-3; ndipo mukhoza kuona ngati mukumva Ahebri akuimba mwacikondwerero, "ndidzayimbira Yehova pakuti wapambanatu; kavalo ndi wokwera wace anawaponya m'nyanja" (ndime 1).

Mu ndime yaciwiri analemekeza Mulungu mu njira yokongola. Nyimbo yacimwemwe inaturuka kucokera mu mitima yao. Yehova ndiye mphamvu yanga ndi nyimbo yanga, ndipo wakhala cipulumutso canga; ameneyo ndiye Mulungu wanga, ndidzamlemekeza; ndiye Mulungu wa kholo langa, ndidzammveketsa. Yehova ndiye wankhondo; Dzina lace ndiye Yehova" (Eksodo 15:2-3).

Miriyamu, mlongo wa Mose, anatsogolera azimai nyimbo ina ya cigonjetso mu ndime 21-22. Azimai anaimba ndi kubvina mwacimwemwe ndi kuthokoza. Iwo analemekeza Mulungu cifukwa cowapulumutsa.

Timapembedza cifukwa timafunitsitsa kupereka zikomo kwa Mulungu. Timaumirizidwa kunena zikomo kwa Mulungu cifukwa ca moyo. kupembedza kwathu pa Mulungu. Francis woyera wa ku Asisi anadziwa tanthauzo la kuyamika. Iye analemba: "zolengedwa zonse za Mulungu ndi Mafumu kwezani mau anu ndi ife imbani aleluya!"

ZINTHU ZOYENERA KUGANIZIRA

Kodi timayamika ndi kuthokoza Mulungu cifukwa ca cigonjetso comwe iye amatipatsa? Mphatso yaikuru ya Mulungu kwa ife ndi cipulumutso copyolera mwa Mwana wace Yesu Kristu. Kupyolera mwa Kristu timapulumutsidwa kucokera ku cilango ca cimo. Kodi ife tikhoza kuthokoza Mulungu motani cifukwa ca mphatso yace yodabwitsa? Kodi kupembedza ndi "kuthokoza" kapena "kulemekeza" kwa Mulungu? Kodi tikhoza kuthokoza Mulungu m'mapemphero ndi m'nyimbo? Kumbukirani kuyamika ndi kuthokoza Mulungu sabata ino cifukwa ca cigonjetso pa cimo.

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Mulungu amafuna kuti ife tikhale aufulu kucokera ku cimo. Mphatso yaufulu ya cipulumutso imacokera kwa Mulungu mwini. Ife sitiyenera mphatso imeneyi. Koma, iye amatipatsa cifukwa amatikonda ife.

2. Tiyenera kuthokoza Mulungu cifukwa ca mphatso ya cipulumutso ndi cigonjetso pa cimo. Iye amatithandiza kugonjetsa macimo mkati mwa miyoyo yathu.

3. Cifukwa ca ukuru wa Mulungu kwa ife, tiyenera kufuna kumupembedza iye.



Aisrayeli anali kukhala ku Kanani tsopano. Iwo sanali kuyenda yenda monga adacita atate ao. Iwo anakhazikika pa malo amodzi nakhala alimi. Iwo anayamba kukhala ngati anthu owazungulira. Ambiri anayamba kupembedza milungu yonama.

Aisrayeli anaiwala Mulungu wa makolo ao. Iwo anaiwala kuti Mulungu anaombola makolo ao kucokera ku ukapolo wa ku Aigupto. Iwo anaiwala kuti Mulungu anawapatsa dziko lamalonjezano.

Kodi ndi ciani ku ciyanjano ca Aisrayeli ndi Mulungu? Kodi iwo adapembedza yani? Kodi Mulungu anamva ciani pakusowa kwao kwa cikhulupiriro?

(Werengani Oweruza 2:13-23 mokweza)

AISRAYELI APEMBEDZA MILUNGU YONAMA

Aisrayeli anafulatira Mulungu. Anayamba kupembedza milungu iwiri ya Akanani yochedwa Baala ndi Asitaroti. Baala anatanthauza "Ambuye adziko." Akanani anaganizira kuti Baala anawapatsa zokolora zabwino. Baala anali wa mwamuna Asitaroti anali wa mkazi. Iwo anakhulupirira kuti milungu ili ndi cifuniro ca banja. Akanani anali kumacita nchito zoipa za cigololo monga mapembedzo ao a Baala.

Ngati kunali mvula ndi zokolola za bwino, Aisrayeli anali kupembedza Baala. Cikhulupiriro ca Aisrayeli mwa Mulungu cinafooka. Macitidwe ao a zigololo anapambana. Iwo anatsata milungu yonama.

PHUNZIRO 9

## MABVUTO POSUNGA PANGANO

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Oweruza 1-3

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Oweruza 2:13-23

MAU APAMTIMA: "Ndipo ana a Israyeli anacita coipa pamaso pa Yehova, naiwala Yehova Mulungu wao."

Oweruza 3:7

Pamene ine ndinali mwana wamng'ono, ndinali kukonda kuthamanga mu chalichi. Mapazi anga anali kucita phokoso lalikuru pamene ndinali kuthamanga! Amai anga sanali kukonda kuti ine ndidzicita cimeneci. Motero madzulo a sabata ina, amai anati, tsopano lonjezo kuti sudzathamanganso mu chalichi. Mulungu salora ana kucita izi cifukwa sizionetsa ulemu m'nyumba ya Mulungu mu mpingo." Motero ndidalonjeza mokhulupirika kuti sindidzathamanganso mu chalichi. Motero titatha kupemphera ndidaiwala malonjezo anga! Ndidayamba kuthamanga ndikuterera ndi kugwa! Ndidagunditsa mutu pansi ndi kukomoka! Pamene ndidauka, ndidaona mai. Ndidakumbukira lonjezano lomwe ndidaphwanya, ndipo sindidathamangenso mu chalichi.

Ndikwapafupi kuphwanya malonjezano. Ndikwapatali kusunga malonjezano. Pamene ife tibvomereza Yesu, timamuitana kuti akhale mu miyoyo yathu. Kubvomereza Yesu ndi cakwa munthu yense pa yekha. Palibe wina aliyense angatibvomerezere Yesu. Tiyenera kucita zimenezi ife eni. Ngakhale makolo athu sangathe kukhulupirira m'malo mwathu.



PHUNZIRO 5

## MULUNGU AMAPANGA ANTHU APANGANO

NDIME YOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Deuteronomo 10-12; Eksodo 19-20

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Eksodo 19:2-9; Deuteronomo 11:8-9,18-19

MAU APAMTIMA: "Ndipo tsopano, ngati mudzamvera mau anga ndithu, ndi kusunga cipangano canga ca padera koposa mitundu yonse ya anthu; pakuti dziko lonse lapansi ndi langa; ndipo ndidzakuyesani ufumu wanga wa ansembe, ndi mtundu wopatulika."

Eksodo 19:5-6

Mapangano ndi mbali imodzi yakhalidwe la tsiku ndi tsiku la Afilika ngakhale masiku ano. Pamene m'nyamata ndi mtsikana afuna kukwatirana amalowa m'mapangano wina ndi mnzace ndipo kawiri kawiri ndi mabanja ambali zonse. Mphatso ndalama ndi malonjezano amasinthana kawiri kawiri. Anthu awiri ofuna kukwatirana ndi mabanja ao amalowa mu mapangano. Mbali iliyonse imakhala ndi zoyenereza kuti akwaniritse panganolo.

Mulungu anapangana ndi Aisrayeli. Iye anawapulumutsa kucokera ku Aigupto. Iwo sanalinso akapolo. Mulungu anawapatsa malamulo ace kuphatikiza malamulo khumi. Iye adzakhala Mulungu wao ndipo iwo adzakhala anthu ace. Mulungu anafuna Aisrayeli kuti abweretse cipulumutso kudziko lonse. Kodi cimeneci cinaoneka motani? Kuti?

(Werengani Eksodo 19:1-9 mokweza)

PANGANO LIPANGIKA

Potsiliza Aisrayeli anafika pa phiri la Sinai. Ulendo wao wocokera ku nyanja yofiira siunali wapafupi. Koma, anacita umboni wa za mphamvu, ndi nkhawa ya Mulungu ya pa iwo. Mulungu anawapulumutsa iwo kucokera ku ukapolo, kucokera ku imfa m'manja mwa Aigupto, ndi kucokera mukumira m'madzi. Ndiponso, iye anawasunga kuti asabvutike ndi njala ndi ludzu mu cipululu.

Anthu anasonkhana mozungulira phiri la Sinai. Ndipo Mose anakwera pamwamba pa phiri. Mulungu anali ndi uthenga wa kwa anthu. Iye anafuna kupanga pangano ndi iwo. Mulungu anapatsa Mose uthenga kuti akauze anthu. Mulungu anauza Aisrayeli kuti amumvere iye (ndime 5). Iwo anali woyenera kusunga pangano ndipo akadakhala cuma capadera ca kwa Mulungu. Iwo akadakhala "Ufumu wa ansembe" (ndime 6). Imodzi ya zinchito za ansembe inali yobweretsa anthu mu ciyanjano ndi Mulungu kupititsa kudziko lonse. Mulungu anafunitsitsa kuti anthu amvere iye. Iye amayembekeza ifenso kuti tidzamumvera.

Kodi Aisrayeli anayankha Mulungu motani?

(Werengani ndime 7-9 mokweza)

UDINDO WA AISRAYELI KWA MULUNGU

Anthu anali kumvera pamene Mose anali kuwauza zomwe Mulungu anali kuyembekeza iwo. Mulungu analamulira kuti iwo adzimumvera iye. Iwo anati "zonse adazilankhula Yehova tidzaci-



Yoswa anagwira nchito kolimba kusunga Aisraye-li kuti akhale wokhulupirika kwa Mulungu.

ZINTHU ZOLINGALIRA

M'gonero wa Ambuye ndi wofanana ndi phwando la paska la Ayuda. Kristu anafera pa mtanda cifukwa ca macimo athu. Mgonero wa Ambuye umatikumbutsa ife zomwe Kristu anacita. Paska anali kukumbutsa Aisrayeli zomwe Mulungu anacitira iwo mu Aigupto. Pamene inu mutenga m'gonero kaciwiri, zimakumbutsa zomwe Kristu anacitira inu.

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Mulungu anatsogolera Aisrayeli kulowa mu Kanani ndi kuwathandiza kugonjetsa dzikolo. Mulungu adzatitsogolera masiku ano ngati titamvera njira zace, ndi kumumvera iye.

2. Aisrayeli anakondwerera paska monga cikumbutso ca ciombolo cao kucokera ku Aigupto. Akristu amasangalala pokhala ndi Mgonero wa Ambuye. Umatikumbutsa ife zomwe Kristu anacitira ife.

3. Pamene Mulungu ali wotsogolera, cigonjetso cimatsimikizika.

Werengani Yoswa 5:10-12 kuti muone momwe Aisrayeli anali kukondwerera phwando la paska.

(Werengani Yoswa 5:10-12 mokweza)

AISRAYELI ATENGA YERIKO

Yeriko unali mzinda umodzi wamphamvu wa Akanani. Unali wozungulidwa ndi cipupa cacikuru. Kodi Aisrayeli akadakhoza kulanda mzinda wotetezedwa motere bwanji?

(Werengani Yoswa 6:1-5 mokweza)

Mulungu adauza Yoswa momwe angagonjetsere Yeriko. Aisrayeli anayenda mozungulira Yeriko masiko asanu ndi awiri. Pa tsiku la cisanu ndi ciwiri anayenda mozungulira m'nzindawo kasanu ndi kawiri. Ansembe asanu ndi awiri anaimba malipenga ndipo cipupa cinagwa. Aisrayeli analanda Yeriko cifukwa anamvera malamulo a Mulungu. Cigonjetso cinali ca Mulungu osati kwa Aisrayeli. Aisrayeli anali kumvera malangizo a Mulungu.

KUMANGA MTUNDU

Mulungu anapitiriza kukhala ndi Aisrayeli. Mulungu anawatsogolera kutenga dziko lonse (Yoswa 11:23). Mulungu anawapatsa cigonjetso.

Potsiriza nkhondo zinatha. Mulungu anasunga malonjezo ace ndi kuwapatsa dziko la malonjezano. Yoswa anali ndi nchito yaikuru yomanga mtundu.

Yoswa anagawa dzikolo pakati pa mitundu khumi ndi iwiri. Kupyolera m'moyo wace wonse,



ta" (ndime 8). Iwo anali okonzekera kulowa m'mapangano. Mulungu anapanga pangano, ndikupanga zoyenereza. Ngati anthu adzamvera malamulo ace, Iye adzakhala Mulungu wao. Iye adzawateteza iwo ndi kuwabweretsa kuti alowe m'dziko la malonjezano la Kanani. Nthano yace inaonetsa kuti Aisrayeli analephera kusunga mbali yao ya pangano. Komabe, Mulungu anasunga mbali yace.

Aisrayeli mwina anali monga ambiri aife lero. Iwo anazindikira njira yabwino, ndipo anadzazidwa ndi kufunitsitsa kozama kuti acite zabwino. Iwo analonjezadi kupembedza Mulungu yekha. Koma analephera. Ife timazindikira njira ya bwino kupyolera mwa Yesu Kristu lero. Koma kodi sitimalephera kawiri kawiri kuyenda njira yolungama? Kodi ife nthawi zonse timamvera Mulungu? Ai, timalephera nthawi zambiri, koma Mulungu anafuna kutikhululukira ife. Iye ali kudikira ife titembenukire kwa iye.

KUYAMBA KWA MAPHUNZIRO ACIKRISTU

Malamulo khumi ndi mapangano ena amalamulo anaperekedwa ndi Mulungu kwa anthu. Koma, iye anapanga malo aciyanjano copitirizira ndi Aisrayeli. Iye analangiza Aisrayeli kuti adziphunzitsa ana ao za iye.

Werengani Deuteronomo 11:18-19. Mulungu anakoza ciphunzitso ca cipembedzo. Anthu anali oyenera kuphunzitsa ana ao za Mulungu ndi mapangano ace a malamulo. Iwo anali oyenera kugwiritsa nchito njira zosiyana siyana kuwathandiza kukumbukira malamulo a Mulungu. Mulungu anauza anthu kuti amange malamulo ace kumanja ao, awabvale pamphumi zao, ndikuwalankhula kawiri kawiri. Mulungu anayembekezera kuti anthu

ace akhale okhulupirika ndi kumumvera iye ndi kuphunzitsa ana ao kuti amumverenso.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Zomwe Mulungu iye amayembekezera ife kuzicita masiko ano. Ife tiri ndi pangano latsopano ndi Mulungu. Mulungu anakhazikitsa pangano lace ndi ife kupyolera mwa Yesu Kristu. Yesu anati, "cikho ici ndi pangano latsopano m'mwazi wanga wothiridwa cifukwa ca inu" (Luka 22:20). Kristu adafera ife. Imeneyo inali mbali ya Mulungu ya pangano la tsopano. Ife tilamulidwa kupereka miyoyo yathu kwa Mulungu ndi kumumvera iye kotheratu. Ife, monga Aisrayeli tiyenera kutsimikizira ana athu coonadi cakuti ciyanjano cao ca kwa Mulungu ndi cofunika koposa mu miyoyo yathu. Tiyenera kugawana cikhulupiriro cathu ndi ana athu. Malamulo a Mulungu ndi cikondi cace ziyenera kulankhulidwa kawiri kawiri mu nkhani zambiri kodi ife tiri monga anthu "apangano latsopano" osunga mbali ya pangano lathu?

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Mulungu anaitana anthu osankhika kupangana ndi iye. Mulungu amaitana ife lero kulowa mupangano ndi iye. Iye amatikonda ndipo afuna ife kuombola mtundu wa anthu.

2. Mulungu analonjeza Aisrayeli dziko loyenda mkaka ndi uci. Iye analonjeza kuti adzawasamalira. Masiku ano "ufumu wa Mulungu" siupezeka m'magawo ambali ya dziko, koma m'mitima ya anthu, amene amalora Mulungu kulamulira mwamphamvu mwa iwo.



Tsopano iwo anali ku gombe la cakum'mawa kwa mtsinje wa Yordani. Iwo anali kunja kwa dziko lamalonjezano. Mose anali atafa. Yoswa anali mtsogoleri wina wao watsopano. Anthu anali wodalira utsogoleri wa Mulungu.

CITSIMIKIZO CA MULUNGU CAKUPEZEKA KWACE

Mtsinje wa Yordani unadzaza ndi madzi amvula. Mu nthawi youma mwina Aisrayeli anali kumaoloka. Koma pa nthawi imeneyi ya caka sakadakhoza kusambira madziwo. Yoswa 3 amatiuza kuti pamene ansembe anali kuponda madzi atatenga likasa cozizwitsa cina cidaoneka. Madzi adaimitsidwa ndipo anthu anafulumira akuoloka pa malo ouma (Yoswa 3:14-4:1).

Cimeneci cinali cinthu cokondweretsa Ahebri. Likasa linatsogolera anthu. Linali cizindikiro ca kupezeka kwa Mulungu. Anthu anadziwa kuti Mulungu anali kupita patsogolo pao ndipo cikhulupiriro cao cidapambana. Kodi iwo anayankha motani ku cinthu cimeneci?

(Werengani Yoswa 4:4-7 mokweza)

Yoswa anasankha anthu kucokera ku pfuko liri lonse. Munthu aliyense anatola mwala kucokera pakati pansi pa mtsinje. Iwo anamanga pocitira nsembe ya miyala. Guwalo linali lokumbutsa zomwe zinacitika. Yoswa anali kuuza anthu kuti adziuza ana ao pa zomwe zidaoneka tsiku limenelo.

Mulungu anauza anthu kuti adzikumbukira ndi kukhalanso ndi phwando. Paska anakumbutsa Ahebri ciombolo ca Mulungu potuluka mu Aigupto.

Mulungu akwaife.

3. Ngati tipempha Mulungu, adzatikhululukira ife. Koma tikhoza kuyembekeza Mulungu kutilanga ngati ife sitimukhulupirira ndi kumumvera iye.

4. Pemphero liri ndi mphamvu yaikuru kwa Mulungu.

PHUNZIRO 8

KUKWERA DZIKO LA MALONJEZANO

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Yoswa 3-6; 14:1-5

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Yoswa 4:4-7; 5:10-12 Yoswa 6:1-5, 11:23

MAU APAMTIMA: "Khala wamphamvu, nulimbike mtima, usaope, kapena kutenga nkhawa, pakuti Yehova Mulungu wako ali ndi iwe kuli konse umukako."
Yoswa 1:9

Kufunitsitsa kwa kupambana ndi kukhala ndi dziko zimakhala m'mitima ya anthu. Kulimbira dziko kwapangitsa nkhondo ndi kukangana kwambiri. Ahebri ayenera kuti analimbirira dziko lomwe linali lao. Iwo anafuna kuti adzale mbeu zao ndikudzimangira nyumba zao. Kwa zaka makumi anayi anali kuyenda yenda mucipululu cosabala kanthu. Mulungu anali kuwapatsa mana monga cakudya ca tsiku ndi tsiku.



3. Aisrayeli anayembekezedwa kukhala okhulupirika kwa Mulungu ndikumvera malamulo ace. Masiku ano ife monga Akristu tiyembekezedwa kukhala monga Kristu analamulira, ndikumumvera iye mu mbali ya miyoyo yathu yonse.

PHUNZIRO 6

ANTHU OPEMBEDZA

NDIME ZOWELENGERA KUNYUMBA: Eksodo 33:1-35; 29; 40

NDIME ZA PHUNZIRO LALERO: Eksodo 33:9-16; 35:29

MAU APAMTIMA: "Ndipo anati, "Nkhope yanga idzamuka nawe, ndipo ndidzakupumuza."
Eksodo 33: 14

Munthu ndi wacipembedzo. Iye amapembedza Mulungu amene anamupanga kapena amapanga Mulungu woti amupembedze. Aisrayeli anakhala ku phiri nthawi yaitali, akulankhulana ndi Mulungu. Iwo anafuna kupembedza. Motero iwo anacita ciani.

(Werengani Eksodo 32:1 mokweza)

ANTHU AMAFANO

Mose sanali kumeneko kuti atsogolere anthu pofuna kupembedza Mulungu. Motero anaganizira kupanga Mulungu wao monga amene anamuona akupembedzedwa mu Aigupto. Anthu anapempha

Aroni kuti awapangire mulungu. Aroni anapanga mwana wa ng'ombe wa golidi kucokera mu ndolo, ndi zigwinjiri za Aisrayeli zomwe anali kubvala. Aisrayeli anapembedza mwana wa ng'ombe wa golidi. Aisrayeli anacita izi patangopita nthawi yocepa Mulungu atawaombola kuwatulutsa. Kodi izi zitiuza kanthu kena za khalidwe la munthu? Kodi ife, lero, timaiwala zomwe Mulungu waticitira ife ndikutembenukira kuzosankha zathu (ndalama, nchito, ndi zina)? Kupyolera mu nthano yoyamba, Israyeli anayesedwa, ndipo kawiri kawiri kudzipereka kupembedza milungu ina molingana ndi zomwe zimacitika mowazungulira. Koma Mulungu anapitiriza kukhala wokhulupilika ku lonjezano ndipo anakhululukira a Israyeli cifukwa cosakhulupirika kwace.

(Werengani Eksodo 33:9-16 mokweza)

MULUNGU AKHALA NDI ISRAYELI

Cizindikiro cimodzi cakuti Mulungu anali kukhala nao panthawi ya mucipululu cinali "hema lokomanira." "Hema lokomanira" limeneli linali lomasunthidwa momwe "likasa" la Mulungu linali kukhala. Iye anali kukhala m'menemo ndi anthu ace panthawi imene anali kuyenda yenda mu cipululu. Mose anali kukomana ndi Mulungu m'menemo. Mulungu anaonetsera ulemerero wace mu hema nthawi ndi nthawi.

Ndime 7 imanena kuti hema linali kutali ndi komwe anthu anali kukhala. Aisrayeli anaona kuti Mulungu anali woyera kwambiri kotero kuti anthu sakanatha kubwera pafupi ndi iye. Mtambo wakucha pakhomo wa pa citseko ca likasa udaonetsa kupezeka kwa Mulungu mkati. Mutambo womwewu ndi umene unali kuperekeza Aisrayeli



Werengani zokambirana pakati pa Mulungu ndi Mose mu Numeri 14:18-23.

AMBUYE ANAMVA NDI KUKHULULUKIRA

Mulungu anamvera dandaulo la Mose. Iye anakhululukira anthu cifukwa ca Mose. Pemphero la Mose linali ndi mphamvu yaikuru kwa Mulungu. Mapemphero akwa anzathu akhoza kukhala amphamvunso.

Mulungu anakhululukira Israyeli ndipo sanawaononge. Koma, Mulungu analanga Israyeli cifukwa anali cikhulupiriro cokwanira. Ndi Aisrayeli awiri okha amene anaturuka mu Aigupto omwe analoledwa kulowa mu dziko la malonjezano. Iwo anali Kalebe ndi Yoswa. Mulungu anapanga Aisrayeli kukhala oyenda yenda mu cipululu kwa zaka 40 kufikira anthu osakhulupirira anafa.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Kodi cikhulupiriro canu ndi colimba motani? Kodi mumaganiza kuti Mulungu samamva mapemphero anu? Kodi mupemphera, kupempha Mulungu kuti akukhululukireni ndikukuthandizani kukhulupirira? Mukacita zimenezi, mudzapeza cigonjetso kupyolera mu mphamvu ya Mulungu.

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA

1. Aisrayeli anataya cikhulupiriro cao pomwe Mulungu anali kuwatsogolera. Ifenso monga Akristu timataya cikhulupiriro cathu mu citsogozo ca Mulungu.
2. Kusoweka kwa cikhulupiriro cathu kudzatilepheletsa kulandira madalitso ocokera kwa

AISRAYELI ANADANDAULA

Aisrayeli anakhulupirira azondi khumi osati Yoswa ndi Kalebe. Iwo anakalipira Mose ndi Aroni. Iwo anafuna kubwereranso ku Aigupto!

Iwo anaganiza kuti adzafera dziko latsopano. Iwo anaganiza kuti anthu a akuruwo adzapha akazi ndi ana ao. Iwo anaiwala momwe Mulungu anawatetezera ndikuwapatsa zosowa. Iwo anafuna kuti asankhe mtsogoleri kuti awatengere ku Aigupto (Numeri 14:4). Iwo anafuna kukhala akapolo ku Aigupto koposa kukhala aufulu pansi pa utsogoleri wa Mulungu!

Aisrayeli analibe cikhulupiriro cokwanira. Motero Mulungu sakadakhoza kuwapatsa madalitso onse omwe anafuna kuti akhale nao. Mose, Aroni, ndi Yoswa ndi Kalebe anayesa kulimbikitsanso cikhulupiriro ca anthu.

(Werengani Numeri 14:4-10 mokweza)

ANTHU SANATSATE MOSE

Aisrayeli sanali kumvera Mose ndi atsogoleri ena. Iwo anafuna kuwalasa miyala. Iwo sanakhulupirira kuti Mulungu akanakhoza kuwapatsa dziko.

Cimeneci cidapanga Mulungu kukhala wokalipira anthu. Iye anauza Mose kuti angopha Aisrayeli. Mose anadandaulira Mulungu kuti asaphe anthuwo. Mose anati dziko lione mphamvu za Mulungu ngati iye angawapatse dziko la malonjezano.



kucokera ku Aigupto. Zinacitika kucokera pamwamba pa phiri la Sinai pamene Mose anakakomana ndi Mulungu. Mtambo udakanganuka kwa kanthawi pamene anthu anapanga fano la mwana wa ng'ombe wa golidi. Anthu analapa. Ndipo tsopano mtambo uja unali cizindikiro cakuti Mulungu analinso ndi anthu aja.

KUPEZEKA KWA MULUNGU KUTSOGOLERA KUPEMBEDZA

Pamene anthu anazindikira kupezeka, kwa Mulungu mu mtambo, anagwa pansi ndikupembedza. Kupembedza kumatanthauza kuti kukomana pakati pa Mulungu ndi munthu. Ndi mbali yofunika koposa ndi Mulungu. Aisrayeli anabvomereza kwathunthu popembedza pamene anazindikira kupezeka kwa Mulungu. Mose adalankhula kwa Mulungu monga bwenzi (ndime 11). Mose anali woimira anthu ace kwa Mulungu. Masiku ano tikhoza kufika kwa Mulungu molunjika kupyolera mwa Kristu. Wokhulupirira aliyense ndi wansembe. Ife ndife ansembe pamaso pa Mulungu ndi kwa wina ndi mnzace. Tiri pa nchito yogwira monga ansembe m'malo mwa anthu anzathu. Kristu naye ndi bwenzi lathu. Yohane 15:15 amanena kuti, "Sindichanso inu akapolo... koma ndacha inu abwenzi; cifukwa zonse zimene ndazimva kwa Atate wanga ndakudziwitsani." Cimodzi ca zozizwitsa ca moyo ndi ubwenzi ndi Mulungu ndi kupezeka ndi anthu wamba monga ife.

MALONJEZO A MULUNGU KWA MOSE

Mose anadziwa kuti Aisrayeli anacimwa. Iye anadziwa kuti iwo anapanga mwana wang'ombe wa golidi ndikumupembedza. Mose anapempha Mulungu kuti awakhululukire (Eksodo 32:13). Mose anadziwa kuti asoweka mphamvu ya Mulungu.

Iye anapempha Mulungu kuti amuonetse njira yace (Eksodo 33:13).

Mulungu analonjeza kukhala ndi Aisrayeli ndi kuwasamalira iwo (Eksodo 33:14). Lonjezano la Mulungu limeneli ndi labwino kwa anthu a Mulungu ngakhale masiku ano. Pamene ife tipembedza Mulungu, iye amalankhula kwa ife. Iye adzatitsogolera ndi kutisamalira ife.

Mose analandira malamulo khumi nthawi yaciwiri. Pamene Mose anaona Aisrayeli akupembedza mwana wa golidi wa ng'ombe, anakwiya kwambiri. Iye anaponya, pansi miyala yomwe idalembedwa malamulo khumi ndi kuaswa (Eksodo 32:19). Mose anabwereranso ku phiri la Sinai. Kaciwiri Mulungu anapatsa Mose malamulo. Mulungu ananenanso kuti anthu sakadayenera kukhala ndi milungu ina. Nchito zonse ziyenera kucitika pa masiku asanu ndi limodzi. Tsiku lacisanu ndi ciwiri ndi tsiku lopembedza Airayeli kuti apange copereka ca kwa Mulungu. Kodi Aisrayeli analora motani kuti acite copereka?

(Werengani Eksodo 35:29 mokweza)

AISRAYELI APEMBEDZA NDI MPHATSO

Mbali ya macitidwe a cipembedzo omwe Aisrayeli anacita anakhoza kupereka. Mose anauza anthu kuti apereke copereka kwa Mulungu. Likasa lacikhalire linapangidwa. Mose anapereka malangizo a kaperekedwe ka mphatso (Eksodo 35:4-29). Iwo anapereka mwaufulu monga momwe mitima yao inawatsogolera kupereka. Iwo anapereka mwakufuna kwao. Kuyankha kwa Aisrayeli kuna kondweletsa ndi kwakukuru



ZOMWE ANANENA AZONDI

Azondi anabwera kudzanena zomwe anaona. Onse anabvomerezana kuti dziko linali labwino. Kunali zipatso zokolora zoculuka ndi madzi. Anthu anali kukhala m'mizinda yabwino ndipo anali kukhala makhalidwe apamwamba.

Koma azondiwo anasiyana pa zomwe anayenera kucita. Kalebe ndi Yoswa anaona kuti akhoza kugonjetsa dzikolo. Iwo anadziwa kuti Mulungu akhoza kuwathandiza. Kalebe anati, "Tikwere ndithu ndi kulilandira lathu lathu" (Numeri 13:30).

Azondi khumi enawo anayamba kudandaula. Iwo ananena kuti anthu amudzikomo anali a mphamvu ndipo anali ambiri. Azondi khumi anati anthu anali atali. "Tinaoneka ngati dzinsidze pamaso pao" (ndime 33).

Ciri conse comwe azondi ananena ca zadziko ndi anthu cinali coonadi. Koma anaiwala kanthu kamodzi. Mulungu ndiye anali woyenera kuwapatsa dziko.

Kodi cidasiyanitsa ndi ciani pakati pa anthu awiri ndi zomwe anthu khumi anenena? Mwina mwace. Yoswa ndi Kalebe anali ndi mzimu wosiyana. Iwo anali ndi cikhulupiriro koposa mantha. Cikhulupiriro cimagonjetsa mantha. Cikhulupiriro ndico kulora mau a Mulungu.

Kodi Aisrayeli anakhulupirira ndani? Kodi anacita ciani?

(Werengani Numeri 14:1-3 mokweza)

nthawi zina zotere? (Mateyu 8:23-27; Mateyu 14:15-20, 28-33).

Ifenso nthawi zina timalephera cifukwa timakhala tilibe cikhulupiriro cokwanira. Pamene cikhulupiriro cathu ciri cofooka, timasemphana ndi madalitso omwe Mulungu amafuna kutipatsa ife. Kawiri kawiri Aisrayeli anali kutaya cikhulupiriro cao. Ngakhale kuti Mulungu anali kuwateteza iwo, ndikuwatsogolera modabwitsa pakati pa Aisrayeli, anakhalabe kutali mu cikhulupiriro cao pa nthawi zina. Kodi muli kukumbukira momwe anapangira mwana wa ng'ombe wa golidi womupembedza? (Eksodo 32). Phunziro la lero ndi la za nthawi zina mu nthano ya Ahebri pamene anataya cikhulupiriro cao. Kwa onse amene anacoka ku Aigupto, anali awiri okha amene anakalowa dziko la malonjezano la Kanani.

KUFIKA DZIKO LA MALONJEZANO

Aisrayeli anafika dziko la malonjezano. Mulungu anawauza kuti adzapatsa dziko kwa iwo. Anthu anali kucita mantha. Iwo anafuna Mose atumize anthu akazonde dziko. Ambuye analankhula kwa Mose ndikuti atumize azondi. Mose anatumiza azondi kucokera ku pfuko la banja liri lonse.

Azondiwo anakhala masiku makumi anai mu dziko lamalonjezano. Iwo anasonkhanitsa zipatso kuti akazionetse kwa anthu. Iwo ananena kuti mudzikomo munali anthu ambiri okhalamo. Kodi azondi anali kunena ciani? Kodi Kalebe ndi Yoswa anafuna kucita ciani?

(Werengani Numeri 13:30-33 mokweza)



kotero kuti Mose anapanga malo apadera olandirira mphatso. Pamene anthu a Mulungu apereka mwakufuna kwao, zofunika za nchito ya Mulungu idzakwaniritsidwa bwino.

Mafunidwe akaperekedwe athu ndi ofunika. Wina wace ananena kuti pali njira zitatu zakaperekedwe. Kupereka mosakondwa, kupereka mwa nchito, ndi kupereka mwakuthokoza. Kupereka mosakondwa kumati, "sindikufuna kupereka koma ndiri ndi mantha" kupereka mwa nchito kumati, "ndiyenera kupereka cifukwa ndi nchito yanga." Koma kupereka mothokoza amati, "Ndifuna kupereka." Kupereka mwacithokozo ndi khomo lotseguka la cikondi ca Mulungu. Timalandira cimwemwe cacikuru pamene tipereka cifukwa timakonda Mulungu. Pamene tipereka mwacikondwerero, timapembedza Mulungu.

ZINTHU ZOLINGALIRA

Akristu onse afunika kupembedza. Pamene muli kupembedza, yembekezani kukomana ndi Mulungu. Kupezeka kwace kukhoza kuonekera kupyolera mu kupembedza kwambiri-kuyamika, kupemphera, kuwerenga Buku Lopatulika, ulaliki ndi zina. Kodi ndi zinthu ziti zomwe zimathandiza inu kupembedza? Masiku ano timapembedza Mulungu mu Mzimu. Yesu anati mu Yohane 4:24, "Mulungu ndiye Mzimu, ndipo omulambira Iye ayenera kumlambira mu mzimu ndi m'coonadi" kodi cimeneci citanthauza ciani? Kodi mukupembedza Mulungu mu mzimu wanu? Mu macitidwe anu?

ZOMWE PHUNZIROLI LIKUTIPHUNZITSA IFE

1. Munthu ali ndi cosowa ca kupembedza Akristu.

Ayenera kupembedza Mulungu wa moyo tsiku ndi tsiku.

2. Popembedza, munthu amakumana ndi Mulungu. Mulungu amalankhula kwa amene akupembedza Iye.

3. Aisrayeli anapereka zopereka monga mbali ya kupembedza yao. Akristu ayenera kupereka mwaufulu monga mbali ya kupembedza.

4. Mulungu adzatitsogolera tsiku ndi tsiku, monga momwe adalonjezera Aisrayeli. Aisrayeli anali anthu a Mulungu mu Cipangano Cakale. Masiku ano Akristu ndi anthu a Mulungu.

5. Anthu a Mulungu ayenera kupembedza Mulungu mu mzimu ndi mu coonadi.



## PHUNZIRO 7

## KUSAKHULUPIRIRA KUMACEDWETSA KUKWANIRITSA KWA PANGANO

NDIME ZOPHUNZIRIRA KUNYUMBA: Numeri 13-14

NDIME ZAPHUNZIRO LALERO: Numeri 13:30-33, 14:1-3, 8-10

MAU APAMTIMA: "Ndipo Yehova anati kwa Mose, anthu awa adzaleka liti kundinyoza? Ndipo adzayamba liti kundikhulupirira, cinkana zizindikiro zonse ndinazicita pakati pao?"
Nemeri 14:11

Bambo anali kusewera ndi mwana wace wa zaka ziwiri. Iye anali kumuika pa tebulo ndi kumunyamula mwamsanga. Mwana anali kuseka. Ndipo bamboyo anali kuimiritsa mwana pa tebulo ndi kunena kuti, "tsopano mwana wanga dumpha! Bambo akuwakha!" Koma mwanayo sanali kudumpha. Iye anakonda atate ace, koma sanawakhulupirire kuti atate akhoza kumuwakha. Atate anamulamula kudumpha, dumpha! Potsiriza, mwana anadumpha ndipo atate anamuwakha iye. Cikhulupiriro cace cinamupangitsa kuti acedwe kumvera atate. Koma pamene anamvera atate ace, ndi kudumpha, pamenepo atate anakwaniritsa lonjezano lace. Iye anamugwira iye.

Yesu pa nthawi yautumiki wace anati, "Anthu inu acikhulupiriro cacing'ono" (Mateyu 8:28), kwa akuphunzira ace nthawi zambiri. Ngakhale kuti zozizwitsa ndi nchito zambiri zomwe ophunzira anaziona, kawiri kawiri analibe cikhulupiriro. Kodi inu mukhoza kukumbukira